**UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO**

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

**NYENGO MSABATAYI**

**KUYAMBIRA PA 9 MPAKA PA 15 SEPTEMBER, 2024**

## NYENGO YA KUTSOGOLOKU

Mawa lolemba pa 9 September, 2024, tiyembekezere nyengo ya mphepo, yamitambo yapatali patali komanso yotentha. Izi ndi kamba ka mpweya ofunda ochokera kumvuma. Koma kuyambira Lachiwiri pa 10 September, mpaka lachinayi pa 12 September, 2024 kudzakhala kwa nyengo yamphepo, yamitambo, yozizila komanso yamvula yamawawa. Izi ndi chifukwa cha mphepo zozizila komanso zachinyotho chochepa zochokera kum'mwera cha kumvuma. ***Mphepo za mvuma ziziomba pa Nyanja koma kuyambira lachiwiri mpaka lachinayi mphepo ya Mwera ikuyembekezereka kuomba mwamphanvu ndi liwiro loposa 50km/hr***.

M'mwezi wa September, madera ambiri kukhala mlingo wokhazikika wakazizilidwe. (**onani Chithunzi-chakumanzere**). Mlingo wokhazikika wa kazizilidwe m'mwezi wa September umakhala pakati pa madigiri **11.2°C** ndi **20.4°C** **(onani Chithunzi-chakumanja)**





*Figure 1 Kaziziridwe komwe kakuyembekezeka mu mwezi wa September (Kumamzere). Mmene mwezi wa September umazizilira (Kumanja)*

## NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

Kunali kwa nyengo yamphepo, yamitambo komanso kunazizira kwambiri m'sabatayi makamaka nthawi ya ku m'mawa. Ndipo ma digiri anatsika kufika pa mlingo wa **6.4 Celcius** ku Mzuzu pa 5 September, 2024. **Kunatentha kwambiri m'madera ambiri ndipo kwa Ngabu kunafika madigiri 35.4 Celcius pa 7 September, 2024.**

## MALANGIZO M'SABATALI

- Asodzi ndi ena ogwiritsa ntchito nyanja akhale osamala pomwe mphepo ya mphamvu ikuomba.
- Tizivala zovala mokwanira komanso tionetsetse kuti ana ndi okalamba akutetezedwa kuchisanu.
- Tipewe kuotha kapena kugwiritsa ntchito mbaula mawindo ndi zitseko zili zotseka.

***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:*** *The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*

**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 8 September, 2024**